

INE SINDIDZALANKHULA ZINTHU ZIMENE MULUNGU SANAZIIKE MWA INE

BEN HOWARD

©2009 Ufulu wonse ndi wotetezedwa. Bukhu iri silingagulitsidwe, kapena mwa njira iriyonse kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama. Silingachulukitsidwe, kapena kutanthauziridwa mu zilankhulo zina popanda chilolezo cholembedwa kuchokera kwa:

Ben Howard
Sound Of Liberty
7286 Hwy 53W
Dawsonville, Georgia 30534 (USA)

Website Address: www.SoundofLiberty.org
Email Address: TwoAnds@SoundofLiberty.org

"Lomasuliridwa Mu Chilankhulo Cha Chichewa"
Ndi
Enoch Kamanula
New Testament Assembly
P.O. Box 64
Mwanza, Malawi

"Ine Sindidzalankhula Zinthu Zimene Mulungu Sanaziike Mwa Ine"
June 22, 2008
Dawsonville, Georgia, USA

INE SINDIDZALANKHULA ZINTHU ZIMENE MULUNGU SANAZIIKE MWA INE

Ine ndikuwerenga ku Bukhu la Aroma, Chaputala cha 15, ndipo ndikufuna nditenge phunziro, **"Ine Sindidzalankhula Zinthu Zimene Mulungu Sanaziike Mwa Ine"** Ine ndikumverera kuti ndizofunika kumanga mkatikati mwa Uthenga uwu chidziwitso chimenecho, kuti tikathe kumvetsa mochuluka chimene Mulungu wapereka mu nthawi ya munyengo iyi. Chimodzi mwa zifukwa uthenga uwu uli wofunika ndi chakuti… ife tikuwubweretsa mu nthawi ino, kufika ku nyengo yathu ya nthawi; chifukwa pali "mipingo," yochuluka makamaka pali mazana a iwo amene amakhulupirira M'bale William Branham ndipo ndizabwino, ife timakhulupiriranso M'bale Branham. Koma nkhani ndi yakuti – M'bale Branham analankhula zinthu zambiri zabwino, koma mu zinthu zambiri Mulungu anamulora iye kuona kutali. Cholinga chinali.., chakuti iye anali Mneneri wofanana ndi aneneri a ku Chipangano Chakale ndi mzimu wa Eliya pa iye ndipo anabwera kudzatsogolera kubwera kwa Ambuye mu nthawi ino yotsiriza. Koma anthu ambiri anaphonya kubwera kwa Khristu mu uzimu ngati Mngelo Wamkulu wa ku Chivumbulutso Chaputala 10, pamene Iye anabwera. Monga m'mene Ayuda anaphonyera kubwera Kwake nthawi yoyamba imene Iye anabwera. Kotero funso langa ndilakuti, "Kodi ife taphonya kubwera Kwake?" Ndi zachisoni kulankhula kuti ambiri aphonya kubwera Kwake kwa Uzimu ndipo iwo adzakhala kwathunthu osakonzekera kubwera Kwake mu thupi.

Nthawi zambiri M'bale Branham amatha kunena, "Mau samabwera kwa aliyense koma mneneri, ndipo Mulungu amakhala ndi mneneri m'modzi pa nthawi imodzi." Chabwino, izo zinali zolondola mu nthawi yake, chifukwa Mulungu amayang'ana Uthenga ndipo iye Mulungu anamulora kulankhula zinthu zimenezo. Inu mukuona Mulungu amadziwa kuti kutsogolo kwake Iye adzazikonza pamene cholinga chake chidzakwaniritsidwa. Ichi anachita kumapeto kwa 1969 pamene ndinayamba kusala kudya kwanga masiku makumi anai. Tsiku la 38 la kusala kudya kwanga Mulungu anabwera mu chipinda ndi mau omveka (monga anachitira ku Edeni ndi Adamu) ndi kupereka uthenga ndipo uthengawo unali wokhudza M'bale Branham kukhala monga aneneri a ku Chipangano Chakale. Zitatha izi ndinalemba Bukhu ndikulitcha, "Mneneri Wa Ku Chipangano Chakale Abwera Ku M'bado Wa Ku Chipangano Chatsopano." Linalembedwa mu 1970 ndipo zinaonetsera kuti uthenga wa M'bale Branham unali wofanana ndi Utumiki wa ku Chipangano Chakale ndipo sunali wofanana ndi Utumiki wa ku m'bado wa Chipangano Chatsopano umene Paulo analemba ku Aefeso, 4:11 kufotokoza utumiki kukhala ndi maudindo osiyanasiyana asanu amene akudziwika ndi ife ngati Utumiki Usanu ku ungwiro wa Oyeramtima. Munthu wa Mulungu wochokera ku Jeffersonville, dera la Indiana, amene dzina lake linali M'bale Raymond Jackson, wodziwikanso mophweka kuti Junior Jackson atawerenga bukhu limeneli anandilembera kalata yapamwamba kwambiri kufotokoza za kulondora pa vumbulutso lokhudza malo a M'bale Branham, ndipo tiri nayo kalata imeneyo mpaka lero. Komanso kanthawi pang'ono M'bale Jackson anabweretsa banja lake ku Dawsonville, Georgia kudzakhala nafe kwa masiku ochuluka ndi kudzalalikira kuno

ku Chalitchi yathu. Tikatuluka mu msonkhano ife tinali ndi nthawi yabwino kukhala pa chiyanjano, kulankhula ndi kukambirana Mau palimodzi. Ine ndinaphunzira kuchokera kwa M'bale Jackson kuti Mulungu anali atachita naye mbuyomo, ine ndikukhulupirira kuti munali mu 1952 ndipo Mulungu anamuulurira iye zokhudza mzimu wa Eliya kubweranso. Pamene amawerenga ku Bukhu la Luka, Chaputala 1:17 iye anaona kuti mngelo amene analankhulidwa ku Malaki, Chaputala 4:5,6 anangolankhula gawo la lemba lokhudza Yohane ngati Yohane wa mu nthawi yake. Iye anazindikira kuti gawo lachiwiri la lemba limenelo linali lakuti likwaniritsidwe mu nthawi ino yotsiriza. Mu nthawi imeneyo munthu wina wachibale anabwera kudzamuchezera ndi kumuuza za M'bale Branham ndi ulendo wake opita ku Africa ndi zinthu zazikulu zimene Mulungu anali atachita kupyolera mwa iye. M'bale Jackson anati, "Ine ndinalingalira kwa ine ndekha pamene iye amalankhula kuti ngati ziri choncho ndiye kuti uyu ayenera kukhala mneneri uja kukwaniritsa gawo lachiwiri la Malaki, Chaputala 4:5-6. Pa nthawi iyi, iye ndi banja lake anayamba kusonkhana nawo ku Branham Tabernacle ndi kupeza kuti malingaliro ake anali olondora pa zokhudza M'bale Branham. Izi ndithudi zinali zoona, kuti moyo ndi utumiki wa M'bale Branham umapezeka mu malemba 100%. Zinali zonse zitakhazikika kuti ndi chimene Malaki, Chaputala 4:5-6 amatanthauza. Mb'ale Jackson anandifotokozera kuti pamene anawerenga Bukhu langa, "Mneneri Wa Ku Chipangano Chakale Abwera Ku M'bado Wa Ku Chipangano Chatsopano," chinachake chinamukhudza mkati mwake ndipo anati kwa ine, kunali **kupitiriza** chimene Mulungu anali atamuonetsera iye pa zokhudza malo a M'bale Branham mbuyomo mu 1952. Zinali zooneka bwino kwa iye pamene amayamikira ntchito za Mulungu. Kenako, M'bale Jackson ndi banja lake anabweranso kudzalalikira Mau a Mulungu ndi kusonkhana nafe.

Tsopano, M'bale Branham analankhula zinthu zambiri zimene zinasonyeza izi kukhala zoona, kuti utumiki wake unali wamtundu wa ku Chipangano Chakale. Koma ndi zomvetsa chisoni kunena kuti anthu ambiri sakudziwa kuti Mulungu wasuntha vumbulutso iri la kubwera kwa Khristu kubwera ku gawo lina la utumiki. Mulungu atamutenga M'bale Branham kupita kumudzi, Iye anatumiza M'bale Raymond Jackson ndi kuulura zinthu zochuluka zimene zinatsalira zosaululika. Koma monga M'bale Branham, Mulungu anamulora M'bale Jackson kuona gawo la Mau limene iye amayenera kufotokoza.., zitatha izi iye amatha kungopereka maganizo ake pa zimene malemba ena amatanthauza. M'bale Jackson anati Chisindikizo cha chisanu ndi chiwiri sichinamasulidwe, Mngelo Wamkulu sanafike, pamodzi ndi zinthu zina, kulankhula za izo monga iye anazionera mu tsiku lake, osadziwa kuti patsogolo zidzamveka bwino pamene Mulungu akupereka chidziwitso kwa Mkwatibwi kupyolera mu Utumiki uwu. Onsewa M'bale Branham komanso M'bale Jackson anagwira ntchito yabwino kutsiriza ntchito imene Mulungu anawaikira kuti ayichite. Tsopano pali anthu amene akulankhula pa zokhudza zinthu zimene M'bale Jackson analemba ndi kulalikira, kuti iye anali ndi "Atero Ambuye" kotero iye asanalembe chirichonse ngakhale kukhala ndi chirichonse cholembedwa, ndipo chirichonse chimene iye analankhula chinali changwiro ndipo sichingasinthike ndipo sizingasinthike. Chabwino, sizingasinthike,

koma ife tipitirira ndi Mulungu monga choonadi chonse chiripo kwa Mkazi wa Khristu mu nthawi ino.

Tsopano poti maziko a chimene tikufuna kuona akhazikika, ife tiziona izo mu malemba monga Paulo anapitira ndi Uthenga kuchokera kwa Yesu Khristu umene unali ndi cholinga chapadera. Pamene tikuwerenga izi, ife tiona kuti Petro analankhula zinthu zina ndipo anabweretsa choonadi, koma sanazifikitse motalika monga Paulo anazifikitsira. Petro analankhula za kubwera kwa Ambuye, koma iye analankhula za kubwera kwa Ambuye ngati kuti Iye adzatsika kuchokera Kumwamba kudzayamba Mileniamu. Zimenezo ziri ku Machitidwe, Chaputala 3. Pamene iye anafunsidwa za kubwera kwa Ambuye, iye anafotokoza m'mene zidzakhalire, ndipo zidzakhala mu njira imeneyo. Koma pali chinsinsi pakati pa kubwera kwake mu thupi ndi Mkwatulo. Uku ndi kubwera Kwake ngati Mngelo Wankulu. (Chivumbulutso 10:1) Ife tikuona kuti uthenga wa Paulo unaonetsera kubwera kwa Ambuye mwa vumbulutso.

Inde, Paulo analankhula za zinthu zofanana ndi Ukwati wa Mwanawankhosa, Khristu ndi Mkwatibwi, ndi Paulo yekha amene anabweretsa vumbulutso limenelo. Ndipo zimayenera kukhala mu njira imeneyo, chifukwa iye samadalira pa chirichonse koma chokhacho chimene Mulungu anamupatsa iye, chimene Mulungu amamuuza. Poona kuti tabwereranso ku nthawi imeneyo pamene kuli ukwati umene ukuchitika, ife tikhoza kuona zimene Mulungu wachita pogwiritsa ntchito anthu ena ndipo timawapatsa ulemu ndi kuyamika Mulungu chifukwa cha iwo. Koma ife tikuyenera kuona kupyolera pamenepo, kuti tikathe kuona chimene Mulungu akuchita tsopano. Iye akupereka masomphenya kupyolera pamenepo, ndipo vumbulutso lathu lakhala lowala ngali khrustalo. Alemekezeke Ambuye! Ndikudziwa kuti anthu ambiri akukambirana, ndipo adzakhala akukambirana pamene tidzasinthika mu kamphindi, mukutwanima kwa diso. Pamene Mkwatulo udzachitika iwo adzakhala akukambiranabe ngati Chisindikizo chachisanu ndi chiwiri chamasulidwa kapena ayi; koma Mkwatibwi akudziwa. Mulungu waonetsetsa kuti tikhale ndi masomphenya enieni mu nthawi ino. Vumbulutso la Mkwatibwi lidzakhala lowala ngati khrustalo. Mulungu amapereka kwa azitumiki osiyanasiyana ntchito zosiyanasiyana ndi zolinga zosiyanasiyana. Cholinga cha Paulo chinali kutenga anthu kuchokera mwa Amitundu kuti akhale Mkwatibwi Wake, kuti akwatiwe ndi Khristu, kumulumikizitsa Mkwatibwi kwa Khristu; ndipo amayenera kuonetsetsa kuti vumbulutso lake ndi londolora. Iye anati, "*Ine ndaika maziko,*" ndipo iye anaikamo zina zimene aneneri analankhula, ndi zina zimene atumwi Achiyuda analankhula, koma ndi zochepa zimene iye anabwereza. Iye **sanabwereze zolankhula** za Yesu, chifukwa anali Khristu mwa iye kulankhula. Nkhani ndi yakuti.., kodi pali uthenga ngati umenewo lero? Tiyeni tiwerenge malemba ena. Ine ndimalankhula za lemba iri pamene ndimalalikira pa za kudzalidwa kwa Mtengo wa Moyo ndi m'mene Ayuda analowetsedweramo. Ine ndikufuna kuwerenga kuchokera ku Aroma, Chaputala 15:16. Tiyeni tipemphere tisanawerenge. "*Atate wakumwamba, dalitsani Mau awa, dalitsani malingaliro athu, mitima yathu, miyoyo yathu, Ambuye. Ndipo mutipatse malingaliro angwiro monga Mau anu akulankhulira, lorani lingaliro limene linali mwa Khristu likhale mwa inu. OMulungu, ine ndikupemphera kuti mutipatse lingaliro limenelo, ndipo inu munanena kuti kutaya malingaliro athu. Ambuye, ine*

ndikupemphera kuti mutithandize ife kuchotsa malingaliro athu amene ali osiyana ndi zinthu za Mulungu. Tidalitseni Ife, mutidzoze ife, ndipo mudalitse omvera a Mau kuti akalandire chimene inu mukupereka. Mu dzina la Yesu ife tikupemphera, Ameni."

Pamene Paulo akuyamba kuuza Aroma cholinga chake mu moyo wake ndi chimene utumiki wake unali, Aroma, Chaputala 15:16 akuti; "*Kuti ndikhale mtumiki wa Yesu Khristu kwa inu Amitundu."* Tsopano zimenezo ndi zofunika, chifukwa pa vesi 8 akuti, kuti Yesu anali mtumiki wa ku m'dulidwe amene anali Ayuda, kukwaniritsa pangano loperekedwa kwa makolo. Koma apa Paulo akuti, "*Kuti ndikhale mtumiki wa Yesu Khristu kwa inu Amitundu, kulalikira uthenga wa Mulungu."* Tsopano, ngati inu mukufuna kudziwa za uthenga wa Mulungu wa Amitundu, sichinachake chimene chiri chinsinsi chimene inu simungathe kuchidziwa. Ndi chotengeka, ndi chodziwika, ndipo ndi chinachake chimene inu mukhoza kuchimvetsa - *Kuti ndikhale mtumiki wa Yesu Khristu kwa inu Amitundu, kulalikira uthenga wa Mulungu kuti kupereka msembe kwa Amitundu kukalandiridwe, koyeretsedwa ndi Mzimu Woyera."* Taonani ichi akuti…, "Kuti kupereka msembe kwa Amitundu kukhale kolandiridwa." Kodi inu mukufuna kulandiridwa? Pali uthenga umene inu ngati wa Amitundu mukhoza kulandiridwa nawo kwa Mulungu, mukuona. Anthu ambiri amadabwa nazo izi ndi izo, koma Mulungu anaziikira ife ngati tikufuna kuziona izo. Iye anachotsa mavuto athu onse mpakana pamene tikuona, m'mene tingaonere ndi choti tione. Chifukwa ife ngati anthu, posalingalira za mzeru zathu, timakhala ndi masomphenya athu athu. Ine ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha masomphenya anga kuti ndikutha kuona Mau ndipo ndi Mau okha basi, ndipo ndikutha kuona Mau a mu nyengo ya nthawi ino. Ndi chimene Mkwatibwi akuona. Iye akumuona Iye. Iye ali ndi diso pa Iye basi, Iye yekha. Ndipo Iye ndi Mau a tsiku iri. Paulo akuti apa kuti uthenga uwu udzakupangani inu kuvomerezeka ndi Mulungu. Gawo lotsiriza la vesi iri likuti, "*Kuyeretsedwa ndi Mzimu Woyera."* Mzimu Woyera ndi umene umatiyeretsa ife. Mzimu Woyera ndi chiyani? Ndi Khristu mwa inu, Chiyembekezo cha ulemelero! Paulo amawauza Aroma pa za izi zonse, chifukwa Aroma anali kwathunthu Amitundu. Iye samafuna iwo akhale osokonezeka pa zoti achite, choti akhulupirire, kapena koti ayang'ane; chifukwa chipulumutso chawo chinali pa vuto ndipo anagwiritsa ntchito mau oti "mwa ichi inu mudzavomerezedwa ndi Mulungu." Izo ndi zolemera, koma ndi chimene iye analankhula. Phunziro langa ndi "Ine Sindidzalankhula Zinthu Zimene Mulungu Sanaziike Mwa Ine." Paulo ndi amene analankhula izi, "Ine ndikungolankhula za zinthu zimene zinaikidwa mwa ine."

Tiyeni tipite ku vesi 17 ya Aroma, Chaputala 15. "*Chifukwa chache ndiri nacho chodzitamandira cha m'Khristu Yesu ndi zinthu za kwa Mulungu."* Mwa kulankhula kwina, izi ndi zoona kwa ine, izi zimene ndikhale ndikulankhula kwa inu, ndipo ndikhoza kuyamika Mulungu chifukwa cha izo. Tsopano, Vesi 18 ndi kumene ndikufuna kutenga lingaliro langa lotsatira. ***"Pakuti sindingathe kulimba mtima kulankhula zinthu zimene Khristu sanazichita mwa ine zakumveretsa anthu Amitundu, ndi mau ndi ntchito."*** Mulungu Alemekezeke! Mukuona? Paulo anati…, ine sinditaya nthawi yochuluka kulankhula zinthu zina izi, chifukwa Mulungu wandipatsa ine chinthu chapadera choti ndichite, ndicho kuwapanga Amitundu kukhulupirira. Ndipo uthenga wake

sumayenera ku Yerusalemu. Sumayenera. Pali lemba limene ine ndikufuna kuti tiwerenge ku bukhu la Machitidwe. Kuwerenga uku ndikofunika kwambiri pa uthenga wa Paulo ndi kutembenuka mtima kwache iye atakumana ndi kuwala, ndipo anayamba kufotokoza zina mwa zinthu zimene zinachitika. Iye atangobadwanso mwatsopano, iye amafuna kupita nthawi yomweyo kwa anthu a kwawo. Iye anali M'yuda ndipo mpingo unali ku Yerusalemu, kotero uku kunali kuyenda mu thupi pobwerera ku Yerusalemu. Uku kunali kuyenda mu thupi poyang'anira kuti kunali kumene Yesu anachokera, kumenenso Yesu anamwalira, kumene atumwi anali. Kotero ichi chinali chinthu cha chithupithupi kuchichita. Kubwerera ku Yerusalemu kuti akaonetsetse chimene iye akuchita. Kotero iye anapita ku Yerusalemu.

Tiyeni tiwerenge ku Machitidwe, Chaputala 9:26, "*Koma m'mene anafika ku Yerusalemu, anayesa kudziphatika kwa ophunzira; ndipo anamuopa iye onse, osakhulupirira kuti anali ophunzira.*" Saulo (dzina lake linasinthidwa kukhala Paulo) anapita kukachita chiyanjano ndi ophunzira, koma iye sanakhale ndi mwai wabwino pochita zimenezo. Iye anayesera kudzilumikizitsa yekha. "Ichi ndi chimene ndikufuna kuchita," iye anati, "ine ndikufuna kudzilumikizitsa ndekha ndi ophunzira awa. Ine ndikufuna kukhala gawo la chinthu ichi chimene chikuchitika apa. Chifukwa pali uthenga apa, pali mtumwi uyu otchedwa Petro ndipo zinthu zikuyenda bwino, kotero ndi kumene ine ndikufuna kupita ndi kukalumikizana nawo ndikukayambira kumeneko." Vesi 26 akuti, "Ndipo anamuopa iye onse, osakhulupirira kuti anali ophunzira." Iwo amachita mantha kuyanjana naye. Iwo anati, "Ine ndamva kuti uja amatizunza uja watembenuka mtima, koma ine ndikuchita mantha nazo pang'ono." Taonani vesi 27 ndi 28.., "*Koma Barnaba anamtenga, napita naye kwa atumwi, nawafotokozera umo adaonera Ambuye m'njira, ndi kuti analankhula naye, ndi kuti m'Damasiko adanena molimbika mtima m'dzina la Yesu. Ndipo anali pamodzi nawo, nalowa natuluka ku Yerusalemu.*" Taonani ichi **"ku Yerusalemu."** Gwirani lingaliro limenelo, chifukwa chinachake chichitika.

Vesi 29 ndi vesi 30 akuti, *Nanena molimbika mtima m'dzina la Ambuye; ndipo analankhula motsutsana ndi Ahelene; koma anayesayesa kumupha iye. Koma m'mene abale anachidziwa, anapita naye ku Kaisareya, namtumiza achokeko kumka ku Tariso.*" Iwo anamuthamangitsa mu Yerusalemu. Taonani apa – Atangomuchotsa iye, chinachitika ndi chiyani? Vesi 31 akuti, "*Pamenepo ndipo Mpingo wa m'Yudeya lonse ndi Galileya ndi Samaliya unali nawo mtendere, nukhazikika; ndipo unayenda m'kuopa kwa Ambuye ndi chitonthozo cha Mzimu Woyera, nuchuluka.*" Taonani.., iyi inali mipingo ya Chiyuda. Kodi izi zinachitika liti? Kodi iwo anapeza mtendere liti? Mpakana atamuthamangitsa Paulo. Iwo amayenera kumuthamangitsa Paulo, kumuchotsa iye ku Yerusalemu. Tsopano, akuti mipingo ya Chiyuda inakula mu chitonthozo cha Mzimu Woyera nichuruka. Inde, iyi inali mipingo ya Chiyuda ndipo Mulungu anali ndi iwo kwathunthu. Mulungu kupyolera mwa Khristu anali pakati pawo ku Yerusalemu kudalitsa Ayuda ndi kutenga anthu, gulu la Ayuda loti lidzalamulire pamodzi ndi Iye mu Mileniamu mkati komanso kuzungulira Yerusalemu ku pfuko la Chiyuda. Koma Mulungu pozindikira izi zonse koposa m'mene iwo amadziwira, atumwi Achiyuda anati, "Paulo akufuna kuphedwa, tiyeni timuchotse kuno." Nkhani ndi yakuti – apa panali Paulo amene anapita ku Yerusalemu

ndipo anayamba kulalikira; osati uku kokha, osati pa malo awa okha, koma kulikonse kumene iye anapita iye analalikira Khristu kwa Ayuda. Chaputala cha 13 cha Machitidwe akuonetsa m'mene iye anapita ku Masunagoge kukalalikira kwa Ayuda ndipo iwo anakwiya ndipo amafuna kumupha iye. Makamaka, nthawi ina amafuna kumupha pomugenda miyala. (osati mpingo koma anthu a Chiyuda) ndi kumusiya iye wakufa. Koma iye anangosasa fumbi kumapazi ake. Ku Machitidwe, Chaputala 13:51 akuti; *"Koma iwo, m'mene anawansasira fumbi la kumapazi awo anadza ku Ikoniyo."* Apa akuti, "Popeza kuti mwakana Mau kuwachotsa kwa inu." Tamverani chimene anawauza pa vesi 47…, *"Ine ndikupita kwa Amitundu chifukwa ndi kumene Mulungu wandiika ine kunena kuti ukhale kuwala kwa Amitundu kuti ukhale chipulumutso kwa iwo.., kuwalanditsa ku mphamvu ya satana kupita ku mphamvu ya Mulungu."* (Machitidwe 26:17-18) Koma kuli konse kumene Paulo analalikira kwa Ayuda amayenera kusasa fumbi ku mapazi ake; iye amayenera kuchoka pakati pawo. Ndipo uku ku Yerusalemu, ku Yudeya, ndi kozungulira kumeneko, mpingo wa Chiyuda unalibe mtendere mpakana atathana naye Paulo. Iwo anamutumuza iye ku Kaisareya. Ine ndikufuna kuwerenga Machitidwe, Chaputala 9:21 kachiwirinso, **"Ndipo mipingo yonse ku Yudeya ndi Galileya inali ndi mtendere…"** iwo atangomuchotsa Paulo. Chifukwa chiyani? Chifukwa Mulungu samamufuna iye kumeneko. Mulungu anali akupanga dongosolo Lake ndipo Iye anati, "Sizingagwire ntchito mpakana mutamuchotsa Paulo, chifukwa ndiri ndi ntchito naye yina yake. Ntchito ya Paulo sikuno ku Yerusalemu. Ntchito ya Paulo ndi yoti apite kwa Amitundu. Ndi chimene ndinamuuza ine pamene ndinamukantha pa njira yopita ku Damasiko." Koma Paulo anali asanakule mu utumiki. Iye anali asanakule mu zinthu za Ambuye, kotero iye anapita molunjika ku Yerusalemu. Mulungu analora zinthu kuti ziyende moipa, osati kwa iye kokha, koma kwa mipingo ya Chiyuda. Koma atangomuchotsa iye, iwo anali ndi mtendere, anapuma. Ndipo akuti.., ***"Iwo anakhazikika, ndipo anayenda m'kuopa kwa Ambuye ndi chitonthozo cha Mzimu Woyera, nuchuluka."*** Kotero anamuthamangitsa Paulo. Iwo anati, "Paulo malo ako si kuno ku Yerusalemu." Iwo anamuchotsa iye. Iwo sikuti anamutaya kunja. Iwo amamukonda Paulo. Ine ndikuganiza iwo sanamumvetse, chifukwa atangofika mu mzindawo munali mavuto. Mpingo sukuyenda bwino chifukwa panali zionetsero. Chifukwa chiyani? Chifukwa amawauza iwo kuti Khristu anali atamutuma iye ndi kumuuza iye kuti akhale kuwala Amitundu.Atumwi a Chiyuda anali atanena kuti uthenga ukuyenera kupita kwa nkhosa zosochera za nyumba ya Israel yokha basi. Zinali choncho mpakana Khristu analankhula kwa Petro ndi kumuuza iye, "Pita ku nyumba ya Koneliyo," amene anali wa Amitundu ndipo pamene iye anabwerera ku Yerusalemu atumwi anzache anatsutsana naye. Ngakhale ku Chaputala cha 11 cha Machitidwe, Vesi 19 akuti, "Atumwi anapita paliponse kulalikira koma kwa Ayuda okha." Ndi chifukwa chache anali ndi mtendere, chifukwa amalalikira uthenga kwa anthu awo. Inu mukuyenera kukhala pamene Mulungu akufuna kuti mukhale kuti uthenga uyatse moyo wanu. Pali chinachake chokhudza ichi chimene chimamveka bwino. Kotero ngati inu muli gawo la icho; chimamveka mu moyo wanu. Sizinali choncho ku Yerusalemu. Paulo akatchula Amitundu, mipingo ya Chiyuda imasautsika. Iwo amasowa mtendere ndi chitonthozo. Iwo analankhula zina

monga chonchi, "Petro chikuchitika kuno ndi chiyani? Munthu uyu amene wabwera mu mzinda uno, akulankhula za Amitundu. Kodi Ambuye sanakuuzeni; kodi ku Mateyu, Chaputala 10 Ambuye sanakuuzeni kuti musapite kwa Asamaliya, osapita kwa Amitundu, koma pitani ku nkhosa zosochera za banja Israeli? Ndipo apa pali chinachake chimene chalowetsedwa mu mpingo chimene chikutivuta ndi kutipweteka." Kenako iwo anamuthamangitsa Paulo ndipo mipingo inali ndi mtendere ndipo "iwo anakhazikika, ndipo anayenda m'kuopa kwa Ambuye ndi chitonthozo cha Mzimu Woyera, nachuluka." Inde iwo anali mwangwiro mu chifuniro cha Mulungu tsopano – kwathunthu. Mpingo wa Chiyuda unali mu chifuniro cha Mulungu. Zinali ngati kuti Mulungu anati, "Paulo, asiye choncho, usawakhudze." Izi zinali monga mwa masomphenya amene Mulungu anamuonetsera iye.

Mutatsatira m'mene Paulo anadutsira, njira ya choonadi, uthenga, iye anapita ku Korinto ndi ku Aefeso. Iye anapita ku Aefeso ndi kuyamba kulalikira Mau, kwenikweni kwa Ayuda. Pa tsiku la sabata, monga mwambo unaliri, iye amapita ku Sunagoge, ndipo nthawi iliyonse amapanga izi amakhala mu mavuto. Ku Aefeso, iye akupatula anthu (Ine ndinalalikira uthenga mbuyomu wotchedwa – *"Atumwi Opatukana Alandira Mau,"*) chifukwa sakanatha kulalikira mu Masunagoge. Iye amayenera kubwereka nyumba. Izi ziri ku Chaputala cha 19 cha Bukhu la Machitidwe. Iye anabwereka nyumba, nyumba ya sukulu yakale ya winawake Tirano ndi kuwaphunzitsa iwo kwa chaka ndi theka. Chifukwa chiyani sanapite ku Masinagoge? Chifukwa chiyani sanachite monga Ayuda ena onse? Chifukwa chiyani sanachite monga Petro ndi atumwi ena achiyuda kupita ku kachisi nthawi ya kupemphera ndi kukawauza iwo za icho? Ayi, chifukwa umboni wa Paulo ukakhalamo, zikanatha kusokoneza chinthu chonse, chifukwa iye akanatha kuikamo za uthenga wopita kwa Amitundu. Iye amayenera kukhala kuwala kwa Amitundu. Icho chinawataya, ndipo Petro amatha kunena, ine sindikudziwa chirichonse pa izi. "Petro ukutanthauza kuti Paulo akulalikira chinachake chimene iwe sukuchidziwa?" Chabwino, Ambuye anamuonekera iye, mosakaika, ndipo Ambuye anamudalitsa iye, koma tiyeni timuletse iye pamene ali mozungulira anthu a Chiyuda.

Kupitirira ku Chaputala cha 15 cha Machitidwe, Paulo amalalikira Mau ndi kunena kuti Amitundu samayenera kudulidwa, kuti iwo samayenera kusunga lamulo, komanso zinthu zomwe Mose anabweretsa, zambiri za izo sizinali zinthu zoti muchite kuti mukapulumuke. Koma Ayuda awa ku Yerusalemu anali atamva izo. Baibulo likuti Abale anachokera ku Yudeya, amene anali ku dera la Yerusalemu, ndipo anayamba kupita ku msonkhano kumene Paulo amalalikira kwa Amitundu. Iwo anayamba kuwalalikira oyera mtima amenewo. Paulo kwenikweni anati, "Apa pali Abale ena ochokera ku dera la Yerusalemu ndipo ife tikufuna kupereka ulemu kwa iwo ndikuwapatsa iwo mpata kuti alankhule kwa ife. Chinthu choyamba chimene iwo anachita kunali kulalikira kuti pokhapokha inu mutadulidwa ndi kusunga Lamulo la Mose inu simungapulumutsidwe. Izi zinadzutsa moto. Mpingo onse wa Amitundu unali mu chisokonekero. Iwo analankhula za icho ndi kumalingalira za icho kwa masiku ochuluka. Kenako Paulo anati, "Tiyeni tipite ku Yerusalemu ndipo tikaone za chinthu chimenechi." Atafika uko, Baibulo likuti atatsutsana kwa masiku ochuluka iwo

anafika ku mathero. Mathero a zonse anali akuti Amitundu sakuyenera kudulidwa. Inu simukanatha kusakaniza zimene Paulo amalalikira ndi zimene Petro amalalikira osapangitsa chisokonezo. Inu mukayesera kutenga zimene Ayuda amalalikira ndi kuzimangirira ndi zimene Paulo amalalikira, penapake sizimalumikizana bwino. Ndi chifukwa chake Paulo anati **"kulankhula zokhazo zimene Ambuye waikiza mwa ine," chifukwa uwu ndi uthenga wochokera kwa Atate wa Kumwamba!** Izi zipanga Khristu mwa inu. Ndi Khristu mwa inu. Ndi Khristu mwa inu, Chiyembekezo cha Ulemelero. Mulungu Alemekezeke! Iye anawafotokozera anthu kumeneko ku Aroma, Chaputala 15.., "*Ine ndine mtumiki wa Yesu Khristu kwa inu Amitundu.*" Ndipo iye anati, "*Ine <u>ndine</u>* – "chimodzi" – *mtumwi kwa inu Amitundu, ndilemekeza utumiki wanga.*" (Aroma, Chaputala 11:13)

Inu mutayesera kuika ichi mu imodzi mwa misonkhano ya Chiyuda kumeneko, zikhoza kubweretsa chisokonezo. Tsopano zina mwa zinthu zimene ife tikulalikira lero, inu mutati muzitengere ku mipingo yambiri lero, zimakhala ndi chochita chomwecho monga Paulo amalalikira kwa Ayuda. Anthu amene amenena kuti amakhulupirira M'bale Branham amatenga za bukhu iri ndi kutenga za bukhu lina kuchokera ku ena mwa mabukhu ake ndipo iwo amati ngati inu simungatengere mu mabukhu, ndiye kuti inu simumakhulupirira Mneneri. "Chabwino inu mumatuluka – ngati mutalowa." Ziri chomwecho iwo sangakuloreni inu ngati mutapanda kutengera zolembedwa za Mneneri. Kenako inu mukapita kwa otsatira M'bale Jackson. Inu mukawadziwitsa ndi kuwaonetsera mwa Mau kuti amuna asanu ndi awiri sadzabweranso, ndipo amuna asanu ndi awiri abwera kale ndipo apita; inu mukawauza kuti mabingu asanu ndi awiri alankhula kale – inu mumatulutsidwa. Ndi chinthu chomwecho ndi uthenga uwu lero. Ndi chifukwa chakuti Mulungu anamuika M'bale Jackson kuti aulule gawo lachiwiri la Chisindikizo cha chisanu pamene Khristu amachita ndi gawo lina la Mau pogwiritsa ntchito utumiki uwu. Ichi ndi chofanana ndi chimene anachita mu tsiku la Petro. Ngakhale pamene Petro amachita gawo lake, Khristu amachita ndi Paulo pa zokhudza Mkwatibwi wa Amitundu; ndipo ndi chimodzimodzi ndi utumiki uwu lero. Ife tikuyenera kumanga pa Uthenga wa Paulo, osati zokambidwa zimene zasanduka chiphunzitso monga .., "Mau samabwera kwa aliyense koma mneneri," komanso "Amuna asanu ndi awiri **akubwera** kuti adzakhale mabingu," zimene sizikulumikizana ndi maziko a Paulo. Ife tiri mu kusuntha kotsiriza kwa Mulungu pamene inu mumapita molunjika ku Mau osati ku chiphunzitso cha mu mibado ya Mpingo imene inali ndi tsiku lake.

Khristu ali ndi Mkazi mu tsiku iri amene wadzikonzekeretsa yekha. Pamene iwo anamuthamangitsa Paulo, mipingo ya Chiyuda inali itapuma, kenako inakula, kenako inachuluka ndi kuopa Ambuye. Ndi m'mene Mulungu anaziikira izo. Iye amatengako kuchokera kwa Ayuda anthu oti adzalamulire pamodzi ndi iye mu Mileniamu. Koma uthenga wa Paulo unali wotengera kukweza phiri mpaka kwa Amitundu. Kudutsa malire; kupita ku malo amene palibe wina aliyense amene anafikako. Pitani kwa Amitundu. Mulungu Alemekezeke!

Tiyeni tipite ku Aroma, Chaputala 15. Ine ndikufuna kutenga vesi langa la phunziro kachiwirinso, Vesi 18, "*Pakuti sindingathe kulimba mtima kulankhula zinthu zimene Khristu*

sanazichita mwa ine zakumveretsa anthu amitundu, ndi mau ndi ntchito." Ife titati titsatire ulendo wa Paulo mpaka ku Yerusalemu kumene iwo amatsutsana kwa masiku ambiri, ife tikumva iwo akumuuza Paulo, "Choka kuno, pita uko. Ife tikupatsa ichi, Amitundu amenewo sakuyenera kudulidwa. Iwo sakuyenera kusunga lamulo." Koma taonani, Petro sanalankhulepo ngakhale nthawi imodzi kuti iwo Ayuda, samayenera kutero. Chifukwa ichi chinali chikhalidwe cha moyo wao ndipo zikuchitikabe lero ku Israel, mukuona. Apa ndi pamene anthu amatengapo.

Tsopano inu mukuona chifukwa chiyani Paulo amayenera kusenza zonse za izi. Iwo amasunga sabata ndipo akusungabe lero. Koma pamene zinafika kwa Amitundu, Paulo anabweretsa oyeramtima palimodzi pa tsiku loyamba la sabata, limene ife tsopano timalitchula Lamulungu kulemekeza chiukitsiro. Ichi Ayuda sakanatha kuchivomereza. Kotero Paulo anachoka ku Yerusalemu wa Ayuda. Uthenga wa Paulo unali chinachake chimene chinali choposa chimene Petro amalalikira, ponena za Amitundu. Sizikutanthauza kuti Uthenga wa Paulo unali waukulu mwa zina, koma anali anthu amene iye anaikizidwira kuti awalalikire ndipo ichi chinapanga kusiyana. Inu mukalankhula motsutsana ndi Petro, inu mukhumudwitsa Ambuye. Chifukwa Petro anali mtumwi wamkulu amene anaima pa tsiku la Pentekosite ndi kunena, "Lapani, batizidwani yense wa inu mu Dzina la Yesu Khristu." (Machitidwe 2:38) Pamene uthenga unabwera kwa Amitundu, zinali mofanana ndi ubatizo wa m'madzi.

Ku Agalatiya, Chaputala 2; Paulo anapita mwa vumbulutso ku Yerusalemu ndi Barnaba. Iwo anali ndi msonkhano waukulu. Akuluakulu onse a mpingo wa Chiyuda anali kumeneko kulankhula zomwe iwo akudziwa ndi chimene Mulungu anachita mwa iwo. Kenako panafika Paulo. Iye anakhala ndi kumvetsera mwa kanthawi pang'ono. Ndadziwa bwanji kuti iye anamvetsera pang'ono? Chifukwa pamene Paulo analemba pazokhudza msonkhano iye anati, "Iwo sanaonjezere chirichonse kwa ine, koma zosemphana…" Iye akanapanda kukhala pansi ndi kumvetsera zimene iwo amalankhula, iye sakanalankhula, "Iwo sanaonjezere chirichonse, koma poona kuti uthenga wa osadulidwa unaikidwa kwa ine, monga uthenga wa m'dulidwe unaikidwa kwa Petro." Powerenga izi mu Chaputala ichi akuti, "Iwo (Atumwi Achiyuda) anandipatsa ine ndi Barnaba dzanja loyenera la chiyanjano" ndipo anati, "Iwe upita kwa anthu akunja." Tsopano, musandiuze kuti Paulo analalikira chinthu chomwecho chimene Petro analalikira, monga Paulo analalikira kwa Amitundu, Petro analalikira kwa Ayuda. Mphamvu ya chipulumutso ya uthenga wa Yesu Khristu ndi yomweyo kaya ndi kwa Ayuda kapena Amitundu. Koma Mulungu anati adzatulutsa kuchokera mwa Amitundu anthu chifukwa cha dzina Lake. Mau amene Paulo anagwiritsa ntchito anali oti Amitundu, ndiye Mkazi wa Khristu, osati Ayuda; Ayuda ndi Abale a Ambuye wathu komanso Mpulumutsi Yesu Khristu. Pali kusiyana pakati pa Mkazi ndi Abale. Abale, Ayuda ali gawo la banja la Mulungu. Iwo adzalamulira mkati komanso kuzungulira Yerusalemu. Yerusalemu adzakhala likulu la dziko lapansi nthawi ya Mileniamu. Koma Khristu akutenga Mkatibwi wa Amitundu monga m'mene Yosefe anachitira ku Aigupto. Unali ukwati wachinsinsi ukuchitika. Abale samadziwa chirichonse pa dziko pa zimene zimachitika ku Aigupto. Chinthu chomwecho chikuchitika ndi Utumiki uwu. **Pali zinthu zina zimene zakhala zikuchitika mu tsiku**

iri ndi ora iri zimene palibe aliyense amene anadziwapo mpakana anapeza Yosefe anali atakwatira. Abale anafika Ukwati utachitika kale, chimene ndi chofanizira ndi Ayuda kubwera kwa Khristu kukwatulidwa kwa Mkazi wa Khristu kutachitika. Inde, Mulungu anatumiza Yosefe ku Aigupto kukasunga moyo ndipo ali komweko iye anatenga mkwatibwi wa Amitundu. Inali nthawi yapamwamba ya ukwati wa chinsinsi monga ife tikudziwira. Iwo samadziwa ngati Yosefe ali ndi moyo kapena wakufa. Winawake anafika kuno posachedwapa ndi kunena, "Ben, ine ndimaganiza kuti unamwalira." Ine ndinati, "Kodi ndikuoneka mwa njira imeneyo?" Iwo samadziwa ngati Yosefe anali wamoyo kapena wakufa. Pamene iwo amaona ngati anali atafa, iye amadzitengera yekha Mkazi wa Amitundu. **Pamene iwo amaona ngati Jeffersonville, Indiana anali malo okhawo kumene chinachake chimachitika, Khristu anali akudzitengera yekha Mkazi wa Amitundu.** Paulo anati iye salankhula zonse zokhudza zinthu zina. Chimene Mulungu wachita kupyolera mwa M'bale Branham, chimene Mulungu wachita kupyolera mwa M'bale Jackson ndi zochuluka ndipo ndi zabwino ndipo ndi zapamwamba, koma tiyeni titenge Mau awa amene tsopano akubwera ndi kusangalala ndi ungwiro uwu.

Kumbukirani pamene Ayuda anamutumiza Paulo ku Kaisareya; mipingo yawo inali mu mtendere kuzunguliro Yerusalemu ndi Yudea. Iyo inakula ndi kuchuluka ndipo iwo anali mu malo a mwambamwamba. Iwo anali atathana naye wosautsa. Sizinali kuti Paulo amatanthauza zowasautsa iwo, koma zinali kuti uthenga wache iye anati Mulungu adzaikamo Amitundu ndipo Mulungu anali atamuika iye kukhala mtumwi kwa iwo. Iwo samatha kuona m'mene zimagwirizanirana ndi zimenezo. Chabwino, Mulungu amadziwa m'mene zikanatha kulumikizana. Anthu ambiri sadziwa m'mene Chisindikizo chachisanu ndi chiwiri chikulumukizana, koma chinamasulidwa pamene zina zisanu ndi ziwiri zinamasulidwa. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, ife takhala tikulandira vumbulutso la izo, monga kumasulidwa kwa Chisindikizo cha chachisanu ndi chiwiri kunapangitsa Kabukhu Kakang'ono kutsegulidwa ndi kubweretsedwa kwa ife mu nthawi ino. Kotero inu mukuona, iwo amene sakuvomereza mfundo yakuti Chisindikizo cha chisanu ndi chiwiri chinamasulidwa sangathe kuona kuti Kabukhu Kakang'ono kanabweretsedwa kwa ife; kupangitsa kusakhala ndi chikhulupiriro kuchitenga icho.

Tsopano Kabukhu Kakang'ono kaperekedwa kwa Mkwatibwi. Ndi chimene ichi chiri. Mulungu anadzutsa munthu kuti ayike maziko kwa Amitundu, palibe aliyense akanachita izi. Ena amati, "Chifukwa chiyani iwe umalankhula mochuluka za Paulo?" Ine sindikutero, koma Mulungu anatero. "Chifukwa chiyani umalankhula za Paulo?" Chabwino, Khristu anaonekera mwa Paulo. Iye anadziika yekha mwa Paulo mpaka Paulo anati, "Tsopano ndikondwera nazo zowawazo chifukwa cha inu, ndipo ndikwaniritsa zoperewera za chisautso cha Khristu." (Akolose 1:24) Iye anandiika ine kukhala mtumiki kunyamula Mau awa." Iye anati, "Ine ndaima pano m'malo mwa Khristu." (2 Akorinto 5:20) Ichi chinali chifukwa chakuti Yesu sakanatha kupitanso kwa Amitundu, chifukwa cha pangano la pfuko la Israeli. Ku Aroma, Chaputala 15:8.., Yesu anali mtumiki wa ku m'dulidwe kukwaniritsa pangano loperekedwa kwa makolo, amene anali Ayuda. Koma Paulo anati, Ine ndine mtumiki wa Yesu Khristu kwa inu

Amitundu." Kotero **"uthenga uwu"** ndi chimodzimodzi chimene Paulo ananena ngati kupereka msembe kwa Amitundu kumene kudzapangitsa wina kulandiridwa kwa Mulungu.

Pali chinthu chimodzi chimene ine ndikufuna ndilowetsemo. Ine ndikufuna inu kuti muone kuti Petro akusowa kuchokera kwa Yesu kupita kwa Paulo mu Chaputala ichi cha 15 cha Aroma. Ku Agalatiya Chaputala 2, iye sakuoneka. Izi zikugwirizana ndi lingaliro lakuti Paulo samafuna apa kulankhula ku Aroma , Chaputala 15 **za zinthu zimene zinali zogwirizana ndi Uthenga umene Khristu anamupatsa iye,** chifukwa amafuna kukhala owonetsetsa kuti ife tilandire uthenga umene iye anatumizidwira kuti adzatenge namwali kuchokera kwa Amitundu kuti akhale Mkazi wa Khristu. Tsopano ndi chimene Uthenga uli. Pamene Paulo anapita ku msonkhano uko ku Yerusalemu sipanatenge nthawi kufikira nthawi imene iwo anamuuza Paulo, "Iwe, pita ukalalikire kwa Amitundu." Ndipo mu tsiku lino, ziri ngati uthenga umene ine ndikulalikira ukuchokera molunjika kuchokera kwa M'bale Branham kufika ku ichi. Koma pali chinsinsi pamenepo kuti Mulungu anali ndi Utumiki kubwera kudzaulura za Abale, Israel – kuonetsera zinthu zochuluka, zina mwa izo ndi zochitika za mu gawo lachiwiri la Chisindikizo Chachisanu, ndi chimene 144, 000 ali, malipenga ndi miliri, mzinda Watsopano wa Yerusalemu. Ine ndikulankhula za utumiki wa M'bale Jackson. Mulungu akusunthabe kupyolera mu uthenga uwu umene ine ndikulalikira ndipo ndiwolondora ndi Mau a Mulungu ndipo ndi "Atero Ambuye!" Ichi ndi cha Mkwatibwi yekha, kumukwatitsa Iye kwa Mwanawankhosa. Ndi chimene chakhala chikuchitika ndipo chikuchitika. Alemekezeke Mulungu!

Mundilore ndiwerengebe, Taonani kuti Paulo anali mtumiki wa Yesu Khristu kwa Amitundu. Kenako akuti, "Ine sindidzayerekeza kulankhula zinthu izo…." Tsopano, ine ndichifukwa chiyani sindikubwereza za M'bale Jackson? Azitumiki ena amafuna kuonetsetsa kuti M'bale Jackson anazilankhula kale izo, kapena ziri mu "Contender" iwo asanalalikire icho. Iwo adzayesera kukhomerera zimene iwo akulankhula pa chimene M'bale Jackson analankhula. Magulu ena adzakhomerera chimene akulankhula powerenga zimene M'bale Branham analankhula. Paulo anati ine sindidzayerekeza kuzivutitsa ndekha mpakana kuti chirichonse chimene ndingalankhule ndikuyenera kuchiyesa ndi chimene M'bale Branham kapena M'bale Jackson analankhula. Taonani tsopano! Ine sindidzayerekeza kulankhula zinthu zimene Mulungu sanaziike mwa ine. Chonde musatenge zimene ine ndikulankhula kuti ndizolakwika kubwereza zimene munthu wa Mulungu analankhula , makamaka iwo amene Mulungu wawagwiritsa ntchito kubwezeretsa chidziwitso choona cha Mau Ake, koma ife sitingakhalire moyo zinthu zimene Mulungu anachita mu dongosolo Lake lobweretsa Mkwatibwi ku malo kumene kukuchitika Ukwati.

Tsopano pamene zinafika ku gawo la Amitundu, Paulo analankhula izi mu njira yomweyo (kumupalitsa) ubwenzi Mkwatibwi kwa Khristu monga mwandimva ine kutumikira mu nthawi yotsiriza kutsiriza kubwera kwa Khristu ndi ukwati wa Mkazi Wake. Monga mukuonera, uthenga uwu unabwera mu magawo atatu; Mfuu, Mau a Mngelo wamkulu, ndi Lipenga la Mulungu limene likuchitika nthawi ino kupyolera mu Utumiki uwu.

Tsopano Paulo sanabwerere ku Mateyu, Marko, Luka, Yohane kulankhula.., "Yesu anati, Yesu anati." Bwanji Paulo akanalankhula za Yesu? Ndiye Paulo akanati, "Inu Amitundu ndinu agalu ndipo mkate, Mau, si anu inu agalu." Iye akanabwereza za Yesu iye akati, "Uthenga uwu si wa inu Amitundu." Inu mukudziwa chiyani? Ndiye kuti uthenga wa Paulo ukanakhala wopanda mphamvu. Chikanakhala chosiyana ndi chimene Mulungu anamuitanira. Paulo analalikira kwa Amitundu monga Khristu "mwa iye" anamuuzira. Iye analalikira kuti panali Thupi kuti tibatizidwiremo. Paulo anaphunzitsa kuti panali mphatso zisanu ndi zinai za Mzimu. Komanso, kuti panali maudindo otumikira asanu mu mpingo. Ndipo ndi atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi. Umenewo ndi utsogoleri wa mpingo, osati ma bishop, maedala, ndi ma dikoni. Maudindo **osankhanawa** ndi chinachake chimene chinapatsidwa ku Mpingo wa kugwa wa Amitundu kugwira ntchito Khristu atachoka pamene Iye anali Kumwamba ngati Wamsembe Wankulu mu nthawi ya mibado isanu ndi iwiri ya Mpingo. Koma Mulungu anamutenga Paulo kupita naye kumudzi, iye anatiuza za Utumiki umene Khristu adzagwiritsa ntchito kubweretsa Mkwatibwi ku kukulansinkhu ndi mkwatulo, ndipo izi zalembedwa ku Aefeso, Chaputala 4:11–16. (Chonde werengani bukhu lathu "Mabishopi, Maedala, Madikoni, ndi Utumiki Usanu kuti muunikiridwe mochuluka.) Nanga bwanji atumwi Khumi ndi awiri? Iwo anali ndi malo awo; koma ife tikulankhula za Uthenga wa Paulo kwa Mkwatibwi wa Khristu amene anali wa kwa Amitundu, osati kwa Abale amene anali Ayuda.

Abale (m'dulidwe wa Amitundu mu nthawi ino amene alibe mitima yodulidwa) **anafika ku Aigupto kudzagula chakudya. Iwo anamva kuti kunali chakudya kumeneko kwinakwake.., pali website yotchedwa SoundOfLiberty.org ku Dawsonville, Georgia, ndipo akuti kuli chakudya. Ndi tirigu wa khwimbi wa kudzikolo. Iwo anamva kuti kunali chakudya kumeneko ndipo Yosefe anali atadzitengera yekha Mkazi kumeneko.** Tsopano Abale amene ndi Ayuda sangasanduke Mkazi. Izi sizikuchotsera aliyense kaya ndi Muyuda kapena Wamitundu amene Mulungu wamuika kubwera kukhala Mkwatibwi. Koma onse, gulu lonse, Ayuda si Mkwatibwi. Iwo ndi Abale.

Aroma, Chaputala 15:19-22 akuti, "*Mu mphamvu ya zizindikiro ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya Mzimu Woyera; kotero kuti ine kuyambira ku Yerusalemu ndi kuzungulirako kufikira ku Iluriko, ndinakwanitsa Uthenga Wabwino wa Khristu; ndipo chotero ndinachiyesa chinthu cha ulemu kulalikira Uthenga Wabwino, pamalopo pamene Khristu asanatchulidwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko a munthu wina.*" **Koma zalembedwa, kumene iye sanatchulidwe, iwo adzaona: ndipo iwo amene sanamve adzamvetsa.** Ameneyo ndi Mkazi wa Khristu pamene Iye akukwatiwa ndi Iye mwa Uthenga uwu. *Chifukwa chachenso ndinaletsedwa kawirikawiri kudza kwa inu."*- (Satana akumumenya mbali zonse zonse.) Mwa kulankhula kwina iwo amatseka makomo awo ku uthenga wapamwamba wa ukwati uwu.

Mu dongosolo la Mulungu pali zinthu zina zimene ife timalankhula zikafika pa – **Ukwati uwu, pamene zifika kwa Amitundu kukwatiwa ndi Khristu, pamene zifika ku Chivumbulutso Chaputala 10, "Ine sindidzayerekeza kulankhula zinthu izo," kapena "ine ndidzalankhula zokhazo zimene Mulungu waulura kwa ine."** Ambuye

akudalitseni inu. Uthenga uwu ukhoza kumangopitirirabe, koma ine ndimafuna kuonetsera kufanana kwake ndi mu tsiku lathu. Chifukwa ngati nditaika chinachake mu tsiku ilo ndi kukuuzani inu chimene Paulo anachita, kapena chimene Petro anachita, kapena chimene wina wake anachita mbuyomo, zingakupindulireni chiyani? Inu mukuyenera kuona kuti ichi ndi (mu nthawi yatsopano) Mau a mu tsiku iri, mu ora iri. Ambuye akudalitseni inu. Tiyeni tipemphere. Atate Wakumwamba, tikukuthokozani, Ambuye, lero chifukwa cha mwai umene mwatipatsa ife kusonkhana mu dzina lanu. Ndipo, Ambuye, ife tikukuyamikani inu ndi kudalitsa dzina Lanu. Ndipo tikukupemphani kuti mupereke kumvetsa kwa wina aliyense wa ife. Mu dzina la Yesu Khristu. Amen.